# ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2026 – 2027

UNITY AND FREEDOM

**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE**
Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo

## LIKOMA
DISTRICT

## Mwachidule

Nyengo ya dzinja ya 2026-2027 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi El Nino wa mphamvu. El Nino ndi kutentha kopyola muyezo kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific zomwe zimakhudza kagwedwe ka mvula dziko lonse.

Boma la Likoma likuyembekezeka kulandila mvula ya mlingo okhazikika kapena kuposela apo mu dzinja la 2026/2027

## October 2026




Mwezi wa October ukuyembekezereka kudzakhala wotentha komaso opanda mvula. Komabe, tiyembekezere mvula ya *Chizimalupsya* ya mlingo osapyola 100mm.

Tiyembekezerenso mphepo ya mkutho ndi ziphaliwali m'mweziwu.

## November 2026




Bomali likuyembekezereka kulandila mvula ya mlingo okhazikika kapena yochepera apo ya pakati pa 50mm kufikira 200mm m'madera ambiri m'mwezi wa November.

Mvulayi ikuyembekezereka kudzakhala ya ziphaliwali ndi mphepo ya mkuntho.

## December 2026




Tiyembekezere mvula yopyola mlingo okhazikika m'mwezi wa December ku Chizumulu komanso ku Likoma. Mvulayi ikuyembekezereka kudzagwa ya mlingo wa pakati pa 250mm ndi 400mm.

Mvula yokhazikika ikuyembekezereka kuyambira sabata loyamba kapena lachiwiri la mwezi wa December.

## January 2027




Mvula ya mlingo wokhazikika kapena woposera apo, ya pakati pa 250mm kufikira 300mm, ikuyembekezeka kudzagwa m'boma la Likoma m'mweziwu.

Mlingo wa mvula umenewu ndi okhazikika kapena oposera apo.

## February 2027




M'mweziwu, tiyembekezere mvula ya mlingo okhazikika.
Mvula yokwana 200mm ikuyembekezereka pa zilumba zonse ziwiri.

Ng'amba yokwana sabata limodzi ikuyembekezereka m'mweziwu.

## March 2027




Mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo yokwana 300mm ikuyembekezereka pa Chilumba cha Likoma ndipo ya pakati pa 150mm ndi 200mm ikuyembekezereka pa chiluma cha Chizumulu.

## April 2027




M'mweziwu, m'madera ambiri akuyembekezereka kudzalandira mvula ya mlingo okhazikika wosapyola 150mm.

Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kudzafika kumapeto pakati pa mwezi wa April.

## DZINJA MWACHIDULE

| Kuyamba kwa mvula yokhazikika | Ngamba | Kutalika kwa nyengo yadzinja | Mathero a mvula dzinja |
|---|---|---|---|
| Mvula yokhazikika ikuyembekezereka kuyambira sabata loyamba kapena lachiwiri la mwezi wa December 2026. | Pali chiopsezo chang'amba yapafupifupi sabata limodzi m'mwezi wa February 2027. | Dzinja lidzakhala masiku apakati pa 130 ndi 140 | Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kudzafika kumapeto pakati pa mwezi wa April. |

| MONTH | NORMAL RANGE | FORECAST |
|---|---|---|
| OCT | 0.0– 0.7 | 8.2 |
| NOV | 8.4– 43.8 | 58.5 |
| DEC | 106.1– 172.4 | 238.6 |
| JAN | 160.5– 247.0 | 208.8 |
| FEB | 159.1 – 194.9 | 146.4 |
| MAR | 168.0– 292.9 | 247.6 |
| APR | 57.2 – 144.6 | 126.8 |




Tebulo ndi galafu zili pamwambapa zikuonetsa kagwedwe ka mvula ku Tukombo CDSS.

**Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:**

ActionFirst · WISER · WFP World Food Programme · UKaid · The Development Fund · Save the Children · IOM UN Migration · The World Bank · Malawi Red Cross Society · World Vision · NCA DCA actalliance

**Tsatilani ulosi ndi malangizo ochokera ku nthambi yoona zanyengo**

For further information contact:
The Director of Climate Change and Meteorological Services,
P.O. Box 1808, Blantyre.
+265 991 69 00 61
metdept@metmalawi.gov.mw
www.metmalawi.gov.mw